



TSIKU LOPEMPHERERA ODWALA-11TH FEBRUARY 2023.

" Msamalireni bwino " Chifundo poyendera Limodzi Musinodi.

Koma Msamariya wina, ali pa ulendo wake, adafikanso pamalo pomwepo. Pamene adaona munthu uja, adamumvera chisoni. Adabwera kwa wovulalayo, nathira mafuta ndi vinyo pa mabala ake, nkuwamanga. Atatero adamkweza pa bulu wake, nkupita naye ku nyumba ya alendo, namsamalira bwino. M'mawâ mwake adatulutsa ndalama ziwiri zasiliva, nazipereka kwa mwini nyumba ya alendoyo. Adamuza kuti, 'Msamalireni bwino, ndipo mukamwazanso ndalama zina, ndidzakubwezerani pobwera.'

' (Luke 10:25-37

Kuyendera limodzi ndi kuthangatana mwaubale ndi nsanamira yofunika pokwaniritsa umoyo wangwiro komanso kuonetsetsa kuti aliyense akukwaniritsa mulingo wamoyo wake kwathunthu. Tisaiwale kuti kalikokha nkanyama tili tiwiri tianthu, pokhala mwaubale, anthu amakondana, kudalirana, kusamalana komanso kulemekezana pozindikira kuti munthu aliyense adalengedwa muchithunzi ndi chifaniziro cha Mulungu. Ngakhale zili chonchi, anthu omwe amakhala mosadalirana ndi kusamalirana, kaya pa mtendere kapena pamabvuto, pamoyo wolimba kapena pamatenda, tanthauzo laumodzi ndi ubale limakhala lopanda tchito. Mdziko komanso Mmpingo, tikuyenera kumakumbukira kuti tili paulendo limodzi, posatengera kupeza kwathu, ndale, kapena kusiyana pachuma. Sizidangochitika mwangozi kuti anthufe tipezeke dera kapena malo amodzi. Chifukwa chakuti timapemphera, kusonkhana ndi kukondwerera Mbuye wathu wouka kwakufa limodzi, ndichizindikiro komanso chikumbutso chakuti tiyenera kumasamalirana nthawi zonse. Tikumbukire mawu a Ambuye wathu akuti, nthawi zonse pamene muchitira chilichonse abale ndi alongo anga nngakhale otsikitsitsa kwabiri, mukuchitira ine amene.

Moyo ndi phukusi la zambiri, matenda kukhala chimodzi mwa izo amaonetsa kufooka kwanth ngati anthu. Ndi chimodzi mwa zithu zakuti ngati tizionera kapena kunyamula tokha popanda abale okuthandizandi kukusamala, matenda amachotsa chiyembekezo ndintanthauzo lamoyo mwamuthu potero amachepetsa kudzikhulupilira yomwe ndi ngodya yofunikira kuti munthu achire.izi zikupherezera mau aja akuti, mutu umodzi susenza denga kapenaso kuti kunyamula mpanda woola nkutengezana. Bvuto mukalionera limodzi, limapepuka". Kusamalira odwala mwaubale ndi chikondi nthawi yamatenda, kumamupatsa odwalayo chilimbikitso chakutu "sindili ndekha mmabvuto awa" zomwe zimabweretsa chiyembekezo ndi kulimba mtima kwa odwala kuti

ndipeza bwino. Ngati Akhristu ndisaiwale nthawi zones kuti ndi udindo wanthu nthawi zones kusamalira abale ndi alongo anthu odwala pamene Mulungu akuwachiritisa. Mchifukwa chake mutu watu wa chaka chino patsiku lopempherera odwala tikuti " *Msamalireni bwino* " **Chifundo poyendera Limodzi Musinodi.**

Ngati Mpingo, tikuyenera tisinkhesinkhe ngati machitidwe anthu komanso chikhalidwe chathu chikuonetsa kuti timalabadako za ubwino wa anthu onse, posamalirana wina ndi mzake makamakanso odwala posatengera kuti ndindani. Posinkhasinkha izi, tikuyenera kulingalira za mau a Ambuye Yesu mfanizo la msamariya wachifundo (Luka 10:25-37). Mpingo ndilo banja la Mulungu, Chifukwa cha Muye wathu Yesu Khristu, amanene amatisokhanitsa pamodzi kudzera mmascrament a Ubatizo, ulimbitso komanso Ukaristia. Chikhalidwe ndi ntchito zathu, zizisonyeza kuti ndifedi abale paulendo umodzi osati anthu osoyana koma oyenda njira imodzi.

Tisaphunzire kufunika kwa ubale ndi kusamalirana Chifukwa chamabvuta ndi matenda ai, koma Chifukwa cha chikondi, ubale,umodzi,kumvetsetsana komwe tingaonetse kwa abale ndi alongo omwe akudwala mdziko komanso muMpingo. Izi siwathandiza kuti naonso aone chithunzi cha Mulungu mwaife ndipo nthawi zones adzakumbukira mau aja a pa Salimo 23 akuti "Chauta ndiye Mbusa wanga;sindidzaopa komanso kusowa kanthu"

Tisaiwale kuwapempherera odwala kudzera mwa uneneri wa Amai anthu Maria, kuti alandire chifundo ndi chisamaliro ndipo aone chikondi cha eni Atatu;Atate, ndi Mwana ndi Mzimu Woyera.

Right Reverend John Alphonsus Ryan,
Bishop of Mzuzu

CHAIRMAN, CATHOLIC HEALTH COMMISSION